## MPHAMVU ZA MKULU WA BUNGWE LOWONA ZOWULULA CHUMA

Mkulu wa bungwe lowona zowulula chuma ali ndi mphamvu izi: -

- Kukhazikitsa kafukufuku pamene pakuganiziridwa kapena pakukayikilidwa kuti lamulo la kawululidwe ka chuma, ngongole ndi mabizinezi la 2013 silinatsatidwe.
- Kulamula kuti kalata kapena umboni ziperekedwe ndi ogwira ntchito m'boma, mabungwe a boma, kampani kapena wina aliyense zokhudzana ndi kuwulula chuma chomwe oyenera kuwulula wapereka.
- Kufunsa oyenera kuwulula chuma kuti akonze zolakwika zokhudza ndondomeko kapena kalembedwe ka fomu yowulurira chuma pasanathe masiku makumi atatu.
- Kuchita zomwe ndi zoyenera kapena zofunika pogwira ntchito yake.

Mkulu wa bungwe lowona zowulula chuma amagwira ntchito zake mosalamulidwa ndi wina aliyense koma amakalongosola ntchitozo ku nyumba ya Malamulo. Mwa ichi mphamvu ndi ntchito za mkuluyu zimatsatidwa ndi komiti yowona momwe zinthu zikuyendera ya ku nyumba ya malamulo.

## Udindo wa anthu pa zowulula chuma.

- Kutsatira bwino kuti ogwira ntchito za boma akuchita zinthu poyera podzawona zomwe adindo awo aulula.
- Anthu ndi ololedwa kuwona chuma chomwe ogwira ntchito m'boma aulula. Kuwona zomwe ogwira ntchito m'boma aulula kumapereka mphamvu kwa anthu kuwunika momwe ogwira ntchito za bomawo akupezera chuma chawo kotero kuti zimalimbikitsa chikhulupiliro cha anthu kwa ogwira ntchito m'boma.
- Pofuna kuwona zomwe ogwira ntchito m'boma awulula munthu amayenera kupempha kwa mkulu wa bungwe la ODPOD polemba fomu yomwe imapezeka ku bungweli yomwenso ili pa tsamba la internet la www.declarations.gov.mw.

## Kutitsina khutu

Aliyense akhoza kumuneneza munthu oyenera kuwulula chuma yemwe wawulula za bodza, wapereka dala zolakwika ngakhale zokayikitsa kwa mkulu wa bungwe lowona zowulula chuma

## Zilango ndi milandu

- Munthu oyenera kuwulula akalephera kupereka mafomu owulula chuma, ngongole ndi bizinezi mu nthawi yoyenera komanso popanda zifukwa zomveka bwino adzachotsedwa ntchito kapena kuchotsedwa pa mpando omwe anamusankha.
- Oyenera kuwulula chuma akapereka mafomu ku ODPOD akudziwa kuti walembamo za bodza akapezeka olakwa adzaponyedwa kundende kwa zaka ziwiri ndi kulipira chindapusa cha K500,000.00 komanso kumuchotsa ntchito m`boma kapena kuchotsedwa pa udindo omwe anasankhidwa.
- Mkulu wa bungwe la ODPOD adzamuwumirizabe oyenera kuwulula chuma, ngongole ndi mabizineziyo kuti apereke mafomu ku ODPOD ngakhale atalandira kale chilango.
- Aliyense ogwiritsa ntchito molakwika zomwe waona mu mafomu owululira chuma, ngongole ndi mabizinezi atapatsidwa chilolezo ndi bungwe la ODPOD adzayimbidwa mlandu, kuponyedwa kundende kwa zaka ziwiri ndi kupereka chindapusa cha K500,000.00 popanda mwayi okasuma kwina kulikonse.

## Zoyenera kutsata powulula chuma

Onse owulula chuma awonetsetse kuti alemba izi pa ma fomu owululira chuma:-

## Mbiri ya munthu: -

- Dzina la bambo,
- Maina ena,
- Tsiku lobadwa,
- Malo ogwira ntchito,
- Udindo wa kuntchito,
- Tsiku loyambira ntchito/kusankhidwa pa ntchito ya boma.

## Katundu ndi zina monga:-

- Katundu yemwe oyenera kuwululayo kapena wachibale wapafupi naye (mkazi, mamuna kapena mwana wake) ali naye chidwi, mtundu wa katunduyo, malo omwe katunduyo ali, tsiku lomwe anagulidwa, ndalama zomwe anagulira, mtengo wakatunduyo pa nthawiyo ndipo ngati nkotheka keyala ya munthu komwe katunduyo anagulidwa.
- Katundu aliyense yemwe oyenera kuwululayo kapena wachibale wapafupi naye wagulitsa kapena kusinthitsa umwini mu miyezi 24 asanalembe pa fomu yowululira chuma, mtundu wa katunduyo, tsiku lomwe anagulitsidwa, kusinthidwa umwini, mtengo wa katunduyo pa nthawi yogulitsayo kapena kusintha umwiniyo ndi kuganiziridwa kuli konse pa nthawi yosinthanayo.
- Katundu aliyense yemwe oyenera kuwululayo kapena wachibale wapafupi naye waperekapo ndalama kapena ndi wake koma mu dzina la wina, mtundu wa katunduyo, komwe katunduyo ali, tsiku lomwe anagulira, kuchuluka kwa ndalama zogulira katunduyo, mtengo wa katunduyo ndi dzina kapena mayina omwe katunduyo ali.
- Ndalama zomwe oyenera kuwulula chumayo kapena wachibale wapafupi naye walandira mu miyezi 12 ya m'mbuyomu, komwe zinachokera, kuchuluka kwake, tsiku ndi kulongosola za ndalamazo.
- Buku laku banki, kuli konse komwe liri, lotsegulidwa mdzina la oyenera kuwululayo kapena pamodzi ndi wachibale wapafupi naye, mnzake, omutumikira, ochita naye bizinezi, ndi dzina la bukulo, dzina la banki, mtundu wa buku, nambala ya buku, ndi ndalama zomwe zili ku bukulo; ndi
- Masheya a mukampani, ndalama zomwe anakongoza ku boma kapena banki yaikulu ya Reserve, mapolicy a inshuransi, kapena ndalama zosungidwa ndi oyenera kuwulula chuma kapena zosungidwa pamodzi ndi wachibale wapafupi naye, omutumikira ngakhale ochita naye bizinezi; ndi komwe ndalamazo zili komanso kuchuluka kwake kwa masheya a mukampani, ndalama zomwe anakongoza ku boma kapena banki yaikulu ya Reserve, mapolicy a inshuransi, ndalama zosungidwa kapena katundu okhudzidwa.
- Ngongole zomwe ali nazo kapena zomwe wachibale wapafupi naye ali nazo komanso dzina ndi keyala ya munthu kapena bungwe lomwe anakatengako ngongoleyo, kuchuluka kwa ngongoleyo, tsiku ndi momwe ngongoleyo inatengedwera.
- Mabizinezi komanso chilichonse chokhudza malonda chomwe oyenera kuwulula chuma kapena wachibale wapafupi naye wachita pa miyezi 24 yapitayo, mtundu wa bizinezi, malo ndi masiku a bizineziyo; ndi
- Tsiku lomwe fomu yowululira chuma yaperekedwa, kusainira kwa owulula chumayo komanso saini ndi chidindo cha mkulu olumbilitsa anthu monga loya.

## Mungatipeze bwanji?

Ngati mukufuna kudziwa zambiri, muli ndi mafunso kapena ndemanga pa nkhani za kawululidwe ka chuma, mukufuna kuwona kalata zowulula chuma kapena mukufuna kutitsina khutu, chonde lumikizanani ndi ofesi ya mkulu owona za kawululidwe ka chuma ya ODPOD pa keyala ndi telefoni izi: -

**Physical Address**

Episcopal Conference of Malawi,
Catholic Secretariat Office Complex, Area 11,
Off Chimutu Road,
City Centre, Lilongwe.

**Postal Address**

Private Bag B 340,
Capital City, Lilongwe 3.
Foni: +265 1 772 673/672
Email: info@declarations.gov.mw
Website: www.declarations.gov.mw

Muthanso kupita ku office iliyonse ya NICE ndikufusa za ODPOD

ODPOD

OFFICE OF THE DIRECTOR OF PUBLIC OFFICERS' DECLARATIONS

# OFFICE OF THE DIRECTOR OF PUBLIC OFFICERS' DECLARATIONS (ODPOD)

## DZIWANI ZA KAWULULIDWE KA CHUMA KWA OGWIRA NTCHITO M'BOMA KU MALAWI



*Omwe anali nawo pa mwambo wa mgwirizano wa ODPOD ndi Financial Intelligence Authority (FIA)*

## Kulimbikitsa Chikhulupiliro Cha Anthu Mwa Ogwira Ntchito Za Boma

## Mawu Oyamba

Bungwe lowona kuti anthu ogwira ntchito za boma akuwulula chuma chawo la Office of the Director of Public Officers Declarations (ODPOD) ndi bungwe la boma loyima palokha lomwe limalimbikitsa kayendetsedwe kabwino ka boma m'Malawi. Linakhazikitsidwa ndi gawo 6 (1) la kawululidwe ka chuma, ngongole ndi bizinezi za ogwira ntchito za boma la Public Officers' (Declaration of Assets Liabilities and Business Interests) Act, 2013. Lamuloli linakhazikitsidwa kuti likwaniritse Gawo 88 A ndi 213 la lamulo lalikulu la dziko la Malawi (Constitution).
Cholinga cha lamulo la kawululidwe kachumali ndi "kupititsa patsogolo chikhulupiliro cha anthu mwa ogwira ntchito za boma kuphatikizapo ena a maudindo a boma ndi osankhidwa pa ndale."

Bungweli liri ndi mtsogoleri komanso wachiwiri wake ndipo onsewa amasankhidwa ndi komiti yowona za kasankhidwe ka anthu ogwira ntchito za boma ku nyumba ya malamulo ya Public Appointments Committee. Iwowa ali ndi udindo owonetsetsa kuti lamulo la kawululidwe ka chuma, ngongole ndi bizinezi likukwaniritsidwa.

## Momwe Bungweli Analipangira ndi Ntchito Zake

Bungweli limakwaniritsa ntchito zake kudzera mu nthambi zinayi zomwe ndi (a) yolandira ndi kusunga kalata zowulula chuma; (b) yotsatira bwino ndi kutsimikizira zomwe zawululidwa; (c) yophunzitsa anthu; ndi (d) yokonza ndondomeko za kagwiridwe ka ntchito, malamulo ndi kuchita kafukufuku. Zina mwa ntchitozi ndi: -

- Kulandira ndi kusunga kalata zowulula chuma zomwe ogwira ntchito za boma omwe ndi oyenera kuwulula apereka.
- Kutsimikizira kuti zomwe zawululidwa mu kalata zoperekedwa ndi ogwira ntchito za boma omwe awulula chuma ndi zoona.
- Kuwonetsetsa kuti lamulo la kawululidwe ka chuma, ngongole ndi bizinezi za ogwira ntchito likufikira kwa anthu mosavuta.
- Kulangiza ogwira ntchito za boma pa za udindo wawo molingana ndi lamulo la kawululidwe ka chuma, ngongole ndi bizinezi za ogwira ntchito za boma.
- Kulangiza njira zoyenera zowululira chuma kwa onse ogwira ntchito za boma omwe ndi oyenera kuwulula.
- Kulengeza mayina a onse ogwira ntchito za boma omwe awulula chuma chawo komanso omwe aswa lamulo polephera kuwulula; ndi kulemba mwachidule chuma chawo chonse mu gazeti ya boma chaka chili chonse.
- Kupereka lipoti, la momwe zinthu zayendera powunika kumvera lamulo kwa ogwira ntchito za boma, kwa nduna ya za chilungamo yomwe imakalipereka ku nyumba ya malamulo.
- Titatsimikizira zomwe anthu awulula, kupereka umboni kapena kukayikira kulikonse pa za umbava wa ogwira ntchito ya boma kwa mkulu owona za milandu, ku polisi kapena mkulu wa bungwe lothana ndi ziphuphu malinga ndi momwe zinthu ziliri.
- Kumuneneza kwa komiti yaku nyumba ya malamulo yowona za momwe zinthu zikuyendera munthu osankhidwa pa ndale, nduna kapena ogwira ntchito za boma oyenera kuwulula chuma, yemwe mukulu wa bungwe la ODPOD, waona kuti komitiyo ichitepo kanthu.

## Cholinga Ndi Ubwino Owulula Chuma

- Zimalimbikitsa ungwiro, kuchita zinthu poyera komanso kawerengetsedwe kabwino ka chuma kwa ogwira ntchito za boma.
- Ndi lamulo loikidwa molingana ndi mbiri yadziko la Malawi ngakhale zomwe zikuchitika pakadali pano pankhani zosamalira chuma cha boma.
- Zimalimbikitsa kuchita zinthu poyera pa ntchito za boma, chikhulupiliro komanso kuvomerezeka kwa boma.
- Zimateteza kukaikilidwa kapena kuganizilidwa zolakwika kuti ogwira ntchito za boma akuba ndalama pogwira ntchito yawo.
- Zimachepetsa mchitidwe wa ziphuphu.

## KODI OYENERA KUWULULA CHUMA NDI ATI?

## Andale Ndi Osankhidwa Pa Mipando

Pulezidenti, Wachiwiri kwa Pulezidenti, Sipikala wa Nyumba ya Malamulo, achiwiri kwa Sipikala wa Nyumba ya Malamulo, Nduna ya boma, Aphungu a nyumba ya malamulo, Mtsogoleri ndi msungichuma wa chipani chomwe chiri ndi phungu mnyumba ya malamulo, Meya ndi makhansala a makhonsolo a m'mizinda, Makhansala a makhonsolo a m'maboma ndi matawuni.

## Akuluakulu A Boma

- Mkulu wa makhothi;
- Attorney General
- Mlembi wa kabineti
- Wachiwiri kwa mlembi wa kabineti
- Majaji a khoti lalikulu komanso la apilo
- A Solicitor General
- Law Commissioner
- Ombudzimani
- Ma Registrar a khoti lalikulu komanso la apilo
- Mkulu owona za milandu mdziko;
- Mkulu ndi wachiwiri wa bungwe lothana ndi ziphuphu la ACB
- Mkulu wa bungwe lowona zowulula chuma
- Mkulu wa apolisi ndi apolisi oyambira udindo wa Superintendent kupita mtsogolo
- A Chancellor ndi Vice Chancellor a yunivesite ya boma
- a Registrar a yunivesite yaboma ndi ogwira tchito zokhudza ndalama
- A komishonala ndi wachiwiri kwa komishonala wa ndende komanso oyang'anira ndende
- Mkulu owona zotuluka ndi kulowa mdziko
- Auditor General
- Mkulu owona zogula katundu wa boma ndi wachiwiri wake
- Komishonala ndi wachiwiri kwa komishonala wa bumgwe lotolera misonkho
- Bwanamkubwa ndi wachiwiri wake
- Mkulu wa gulu la nkhondo, wachiwiri wake ndi asilikali oyambira udindo wa meja kupita mtsogolo
- Administrator General
- Registrar General;
- Alembi a boma ndi achiwiri awo
- Mkhala pa mpando, ma Board Members, a Chief Executive ndi wachiwiri kwa Chief Executive wa bungwe la boma, ma parastatal, ma constitutional body ndi mabungwe onse a boma omwe anawakhazikitsa ndi lamulo la ku nyumba ya malamulo
- Gavanala, wachiwiri wake, Director ndi Manager wa banki yaikulu ya Reserve ku Malawi
- A Chief Executive, achiwiri kwa Chief Executive a khonsolo ya mzinda, boma kapena tawuni
- Akuluakulu a boma a udindo ofanana ndi director kapena oyang'anira dipatimenti.

## Ogwira Ntchito Ena

Ogwira ntchito zogamula milandu ku khothi, owona za kagulidwe ka katundu wa boma; a ku Road Traffic Department; ogwira ntchito ku bungwe lokhometsa misonkho la Malawi Revenue Authority; ogwira ntchito ku Immigration; ma State Advocate, Legal Aid Advocate ndi maloya onse a boma; Traffic Police officers ndi ogwira ntchito yofufuza ku police; opereka uphungu kwa pulezidenti ndi wachiwiri kwa pulezidenti; opereka uphungu kwa nduna ya boma; owerengetsera chuma cha boma; ogwira ntchito ku bungwe la ACB ndi ogwira ntchito ku bungwe lowona za kagulidwe ka katundu wa boma.

## Kalembedwe ka mafomu owululirapo chuma

Pali mitundu itatu ya kawululidwe ka chuma yomwe ogwira ntchito za boma ayenera kutsata powulula chuma chawo. Amawulula ndi kupereka motere: -

## Kuwulula chuma koyambirira

Oyenera kuwulula chuma, yemwe akuwulula chuma chake koyamba amalemba pa fomu ya omwe akuyamba kumene kuwulula chuma.

## Kuwulula chuma kwa pa chaka

Akawulula chuma koyambirira, oyenera kuwulula chuma azipeleka fomu yowululira chuma ya pa chaka, koyambirira kwa chaka chirichonse cha chuma cha boma, mkatikati mwa masiku makumi atatu. Choncho fomu yowululira chuma ya pa chakayi izipelekedwa kuyambira pa 1 July mpaka pa 30 July chaka chili chonse.

## Kuwulula chuma kotsiriza.

Oyenera kuwulula chuma amaulula kotsiriza miyezi itatu isanathe asanasiye ntchito, pokhapokha ngati anapereka fomu yowululira chuma yoyambirira kapena ya pa chaka mkatikati mwa miyezi itatu asanasiye ntchito.
Komabe, akachotsedwa kapena kusiya ntchito mwadzidzidzi, mkulu wa bungwe lowona zowulula chuma akhoza kulamula kuti awulule chuma kotsiriza mkatikati mwa masiku makumi atatu kuchokera pa tsiku lomwe wachotsedwa kapena kusiya ntchito, pokhapokha ngati anawulula chuma koyambirira kapena pa chaka mkatikati mwa miyezi itatu asanachotsedwe kapena kusiya ntchito.
Mtundu uliwonse wa kuwulula chuma uli ndi fomu yake imene oyenera kuwulula chuma amayenera kulembapo.
Mafomu owululira chuma mungawapeze ku ofesi ya ODPOD kapena pa website yomwe ndi www.declarations.gov.mw.



*Mkulu wa ODPOD Mr. Christopher Tukula (patsogolo, achitatu kuchokera ku manja) Wachiwiri kwa mkulu wa ODPOD Mr. Michael Chiusiwa (patsogolo, wachiwiri kuchokera ku manja) Ogwira ntchito ndi achitetezo kujambulitsa pa maphunziro ozimitsa moto*